# DIOCESAN EUCHARISTIC CONGRESS MASTER PROGRAMME

## Thursday, 3rd to Saturday, 5th September, 2026

## THEME: Eucharist: *Source and Summit of Our Christian Life"*

| *DAY* | *MORNING* | *AFTERNOON* | *EVENING* |
|---|---|---|---|
| **Day 1: Thursday 3rd September** | **07:00 – 9:00 hrs.: Final preparation** by the Organizing Committee<br><br>**09:00 – 9:30 hrs – Gathering of attendees for the Opening Ceremony**<br>• Arrival of Bishop, priests, the religious, delegates and the lay faithful<br>• Eucharistic chants and meditative hymns by Chikwawa Parish Choirs<br><br>**9:30 – 10:00 hrs: Processing and Entrance of the Blessed Sacrament** – Chikwawa Parish Choirs and Catholic Charismatic Renewal<br>• Solemn Eucharistic procession accompanied by incense<br>• Enthronement of the Blessed Sacrament on a designated place.<br>• Moment of silent adoration by all gathered.<br><br>**10:00 – 10:30 hrs: Official Opening of the Congress** | **12:45 – 13:45 hrs.: Lunch Break** – Diocesan Functions Committee<br><br>**14:00 – 15:00 hrs: 1st Session:**<br>**Facilitator:** Rev. Fr. John Lockie<br>Theme: *"The Holy Eucharist and Adoration."*<br>**Presenter:** Rev. Fr. Elizeo Nthalika, DP<br>**Choir:** CWA, Chikwawa Parish<br><br>**15:00 – 15:30 hrs - Plenary**<br><br>**16:00 – 17:00 hrs – 2nd Session.**<br>**Facilitator:** Mrs. Flora Kaphantengo<br>**Theme:** "*Eucharist: Source and Summit of Our Christian Life"*<br>**Presenter:** Mrs. Mary Mangwiza Manyusa.<br>**Choir:** CWA, Chikwawa Parish | **17:45 – 18:45 hrs: Adoration: -**<br>**Presider:** Rev. Fr. Stanford Sungani<br>**Assisted by:** Rev. Fr. Matthews Fatch.<br>**Choir:** Chikwawa Parish and Catholic Charismatic Renewal.<br><br>**18:45 - 19:45 hrs: Supper**<br>Diocesan Functions Committee<br><br>**19:45 hrs: Adoration**: Animated by Catholic Charismatic Renewal and their Chaplain |

| | | | |
|---|---|---|---|
| | • Introductions of delegates and attendees by **Rev. Fr. John Lockie**<br>• Logistics by **Rev. Fr. John Lockie**.<br>• Welcome Remarks by the **Parish Priest, Rev. Fr. Lazarus Maloya**<br>• Brief background and purpose of the Congress to Eucharistic Congress and Explanation of the Theme of the Congress by **Chairperson of the Congress, Rev. Fr. Samson Kayuni**<br>• Solemn declaration by **Rt. Rev. Peter Musikuwa** at the Opening of the first diocesan Eucharistic Congress<br><br>**10:30 – 11:00 hrs – Individual Confessions**<br><br>**11:05 hrs: Prayers for preparation for the Holy Mass:**<br><br>**11:15 – 12:30 hrs: Opening Mass:**<br>**Presider:** Rt. Rev. Peter Musikuwa<br>**Facilitator:** Rev. Fr. Mathews Kamiza<br>**Liturgy:** Chikwawa Parish. | **17:00 – 17:30 hrs - Plenary**<br><br>**17:30 – 17:45 hrs. – Preparation for Adoration** | |
| | | | |

| | | | |
|---|---|---|---|
| **Day 2: Friday 4th September** | **08:00 – 9:00 hrs: 3rd Session:**<br>**Facilitator:** Rev. Sr. Ema Kulombe, SBVM<br>**Theme:** *"Eucharist at the Centre of Consecrated Life and our devotion to the Blessed Sacrament."*<br>**Presenter:** Rev. Sr. Elizabeth Namuthuwa, SDP<br>**Choir:** CMA, Chikwawa & Nchalo Parishes<br><br>**09:00 – 9:30 hrs: Plenary:**<br><br>**09:30 -10:30 hrs. 4th Session:**<br>**Facilitator:** Rev. Fr. Emmanuel Malikebu<br>**Theme:** *"Sacrament of Penance and Reconciliation as preparation for the Eucharist."*<br>**Presenter:** Rev. Fr. Stanford Sungani<br>**Choir:** Molere & Chikwawa Parishes<br><br>**10:30 – 11:00 hrs. Plenary**<br><br>**11:00 – 11:15 hrs. Individual Confessions**<br>**Facilitator:** Rev. Fr. John Lockie<br><br>**11:15 – 12:00 hrs: Holy Mass:**<br>**Presider:** Rt. Rev. Peter Musikuwa:<br>**Liturgy:** Molere Parish. | **12:00 – 13:00 hrs: Lunch Break**<br>Diocesan Functions Committee<br><br>**13:00 – 14:00 hrs. 5th Session:**<br>**Facilitator:** Rev. Fr. Benedict Cholomali, DP<br>**Theme:** *"The Holy Eucharist with Family Life."*<br>**Presenter:** Rev. Fr. Cosmas Kinly, DP<br>**Choir:** CMA, Chikwawa & Nchalo Parishes<br><br>**14:00 – 14:30 hrs - Plenary**<br><br>**14:30 hrs. Preparation for Eucharistic Procession**<br><br>**15:00 hrs: Eucharistic Procession: Route:** From Chikwawa Cathedral to St. Lawrence Girls Secondary School.<br>**Designated stations for benediction:** CADECOM, Chikwawa Secondary School & St. | **19:00 hrs: Supper**<br>Diocesan Functions Committee |

| | | | |
|---|---|---|---|
| | | Lawrence Girls Secondary School.<br>**Presider:** Rev. Fr. Shadreck Malata<br>**Assisted by:** Rev. Fr. Alexious Lipenga and Rev. Fr. David July.<br>**Choirs:** Fatima, Bangula and Misomali Parishes. | |
| | | | |
| **Day 3: Saturday, 5th September** | **08:00 - 08:45 hrs: Holy Rosary:** Animated by the Legion of Mary and Divine Mercy Members<br>**Individual Confessions:**<br><br>**08:45 - 09:15 hrs: Presentation of Highlights and Resolutions of the Diocesan Eucharistic Congress.**<br>**Facilitator:** Rev. Fr. John Lockie<br>**Presenter:** Theological Committee.<br><br>**09:15 – 09:30 hrs.: Individual Confessions**<br>**Facilitator:** Rev. Fr. John Lockie<br><br>**09:30 – 11:00 hrs: Closing Mass:**<br>**Presider:** Rt. Rev. Peter Musikuwa:<br>**Facilitator:** Rev. Fr. Mathews Kamiza<br>**Liturgy:** St. Mathew's, Nchalo Parish. | **12:00 – 13:00 hrs: Lunch**<br>Diocesan Functions Committee<br><br>**13:00 hrs: Farewell and Departure** of guests, attendees and delegates | |

| | | | |
|---|---|---|---|
| | **11:00 - 11:30 hrs: Great Commissioning** of delegates by the Diocesan Bishop<br>**Facilitator:** Rev. Fr. Mathews Kamiza<br><br>**11:30 – 12:00 hrs. Group Photos**<br>**Facilitator:** Rev. Fr. John Lockie | | |
| | | | |

**DAY ONE: Thursday, 3rd September, 2026: Mwambo Wotsekulira Msonkhano Waukulu wa Ukaristia**

***Mutu:*** *"Ukaristia: Gwero ndi Chithimethime cha Moyo ndi Utumiki wathu wa Chikhristu." (Eucharist: Source and Summit of Our Christian Life")*

**9:00 – 9:30 hrs – Kusonkhana**

- Episikopi, ansembe, asisitere, a brother, a catechist, nthumwi za magulu achikhristu ndi akhristu onse afika pa malo a msonkhano
- Akwaya akhala akuimba nyimbo za Ukaristia pa nthawi imene anthu akufika.

**9:30 – 10:00 hrs: Mdipiti wolowa ndi Sakramenti Loyerayera la Ukaristia**

1. Nyimbo ya Ukaristia

2. Mdipiti wa Sakramenti Loyerayera la Ukaristia

    i. Wa mtanda ndi onymula makandulo
    ii. Wa chombo ndi lubani / belu
    iii. Wansembe atanyamula Ukaristia mu Monstrance

3. Kukhazika Sakramenti Loyerayera la Ukaristia ndi kupembedza mwachinunu

**10:00 – 10:30 hrs:** **Mwambo wotsekulira msonkhano waukulu wa Ukaristia**

4. Malonje ndi kulengeza zochitika – **Main Facilitator, Rev. Fr. John Lockie**
5. Kuonetsa nthumwi ndi onse amene afika ku Msonkhano waukulu wa Ukaristia - **Main Facilitator, Rev. Fr. John Lockie**
6. Kufotokozera dongosolo la pa malo - **Main Facilitator, Rev. Fr. John Lockie**
7. Mau olandira anthu – **Parish Priest, Rev. Fr. Lazarus Maloya**
8. Kufotokozera mwachidule za mbiri ya msonkhano waukulu wa Ukaristia ndi zolinga zake. - **Chairperson of the Congress, Rev. Fr. Samson Kayuni**
9. Kulengeza za kutsekulira kwa msonkhano waukulu woyamba wa Ukaristia mu dayosizi ya Chikwawa - **Rt. Rev. Peter Musikuwa**
10. Kubwezera Ukaristia mu Tebenakulo – **Wansembe wotsogolera**

**10:30 – 11:00 hrs: -** **Individual Confessions**

**11:05 hrs.** **Mapemphero okonzekera Nsembe ya Ukaristia:**

*Onani Mapemphero okonzekera Nsembe ya Ukaristia pa tsamba 29.*

**11:15 – 12:30 hrs:** **Nsembe ya Ukaristia yotsekulira Msonkhano Waukulu wa Ukaristia.**

*Mau a Mulungu akuchokera pa Lachinai, Mulungu wa 22 pa chaka*

**Mau oyamba:** 1 Akorinto 3:18-23

**Nyimbo ya Salimo:** Salimo 24:1-6

**Mthenga Wabwino:** Luka 5:1-11

**12:45 – 13:45 hrs.:** **Lunch Break**

**14:00 – 15:00 hrs:** **Mutu woyamba:** Rev. Fr. Elizeo Nthalika, DP

"The Holy Eucharist and Adoration."

**15:00 – 15:30 hrs:** **Kukambirana za mutu woyamba:**

**16:00 – 17:00 hrs.:** **Mutu wachiwiri –** Mrs. Mary Mangwiza Manyusa

"Renewal and deepening our faith in the Eucharist." / "Kuyambanso mwatsopano ndi kuzamitsa chikhulupiriro chathu mwa Ambuye Yesu okhala mu Ukaristia."

**17:00 – 17:30 hrs:** **Kukambirana za mutu wachiwiri:**

17:30 - 17:45 hrs.: **Kukonzekera mwambo wa Kupembedza ndi Udalitso**

17:45 - 18:45 hrs.: **Kupembedza ndi Udalitso**

## Dongosolo la Kupembedza ndi Udalitso

1. **Nyimbo ya Ukaristia pamene wansembe akulowa ndi kuika Ukaristia pa guwa**

2. **Kutsekulira mwambo**

**Wansembe:** M'dzina la Atate, ndi la Mwana ndi la Mzimu Woyera.

**Onse:** Amen.

*Kenaka wansembe anena molandizana ndi akhristu katatu kuti:*

**Wansembe:** Atamandike Ambuye Yesu mu Sakramenti Loyerayera la Ukaristia.

**Onse:** Atamandike nthawi zonse.

**Wansembe:** Ulemu ukhale kwa Atate ndi kwa Mwana ndi kwa Mzimu Woyera

**Onse:** Monga panali poyamba ndi tsopano ndi masiku onse ndi pa nthawi zosatha. Amen.

3. **Kulengeza mutu wa kupembedza**

Mutu: **UKARISTIA NDI MAZIKO A MOYO WATHU**

## 4. Malonje

**Wansembe:** Ambuye Yesu, ife timakhulupirira ndi kumvera Inu. Tikumvetsa ndithu kuti Sakramenti la Ukaristia ndi maziko a moyo wathu wachikhristu. Tsiku lirilonse mukutiitana kuti tiyike chiyembekezo chathu mwa Inu kupyolera m'Mau anu komanso koposaposa mu Sakramenti la Ukaristia. Ukaristia ndi Sakramenti la chikondi, komanso la umodzi. Kupembedza ndi njira imodzi yoonetsa chikondi chathu kwa Inu Ambuye Yesu ndikuzamitsa chikhulupiriro chathu mwa Inu. Iyi ndi nthawi ya mtengo wapatali kuti:

- Tikupembedzeni ndi kukubwezerani chikondi chanu.
- Tikuthokozeni pa zonse zimene mumatichitira.
- Tikupepeseni chifukwa chakulephera kwathu posatenga Ukaristia ngati maziko a moyo wathu.
- Tikudziwitseni ndi kukuonetsani kuperewera kwathu mene tiyenera kukusangalatsirani.

Pa nthawi ino tiyeni tipepese Mulungu chifukwa cha kulephera kwathu mwa njira zosiyanasiyana kuti mapemphero athuwa tiwapereke tili ndi mitima yoyera.

Ambuye Yesu tikuti pepani chifukwa:

- Cholephera kukukondani mu Sakramenti la Ukaristia.
- Cholephera kuwadziwitsa ena za chikondi chanu.
- Cholephera kukuyenderani mu Sakramenti lanu loyera.
- Cholephera kuvomereza kukonzanso kuperewera kwathu muzambiri

Ambuye, pa zonsezi tikuti pepani.

5. **Kusinkhasinkha**

6. **Nyimbo ya Ambuye mutichitire chisoni**

*Akwaya atsogolera nyimbo ya Ambuye mutichitire chisoni*

7. **Pemphero**

**Wansembe: Tipemphere:**

Ambuye Yesu, tikukuthokozani chifukwa chakudzipereka nokha kwa ife kuti muzikhala nafe nthawi zonse ndi kumatilimbikitsa moyo wathu wa pansi pano. Tikukuthokozaninso chifukwa mumatilandira pamene tikubwera kwa Inu, tionjezereni chikondi kuti tizikumbukira nthawi zonse kuti popanda chithandizo chanu sitingathe kuchita kanthu pa ife tokha.

**Onse:** Amen

*Onse akhala pansi*

8. **Kusinkhasinkha**

9. **Nyimbo ya Salimo:** Salimo 116:10-12, 13-15, 16-17,18-19.

10. **Kusinkhasinkha**

11. **Nyimbo ya Mzimu Woyera:** No: 43 (1,2,3 ndi 6)

12. **Mthenga Wabwino:** Luka 5:1-11

13. **Kugawa Mau**

**14. Kusinkhasinkha**

**15. Nyimbo ya Ukaristia mavesi atatu**

**16. Litania la Ukaristia**

Ambuye mutichitire chisoni **Ambuye mutichitire chisoni**
Khristu mutichitire chisoni **Khristu mutichitire chisoni**
Ambuye Yesu mutimvere **Ambuye Yesu mutivomereze**
Mulungu Atate akumwamba **Mutichitire chisoni**
Mulungu Mwana Mpulumutsi wa anthu onse **Mutichitire chisoni**
Mulungu Mzimu Woyera **Mutichitire chisoni**
Utatu Woyera ndinu Mulungu m'modzi yekha **Mutichitire chisoni**
Ukaristia woyera **Tikupembedzani**
Mphatso yosaoneka ya Mulungu Atate, **Tikupembedzani**
Chikondi chopanda malire cha Mwana wa Mulungu, **Tikupembedzani**
Chodabwitsa cha chikondi cha Mzimu Woyera, **Tikupembedzani**
Mphatso yoyerayera ya Virgo Maria **Tikupembedzani**
Sakramenti la Thupi ndi Magazi a Yesu Khristu **Tikupembedzani**
Sakramenti lopitiriza Nsembe ija ya pa mtanda **Tikupembedzani**
Sakramenti la chipangano chatsopano ndi chosatha. **Tikupembedzani**
Chikumbutso cha chipulumutso chathu, **Tikupembedzani**
Pwando la 'ukwati wa Mwanawankhosa. **Tikupembedzani**

Yesu mu Ukaristia, Nsembe yoyamika ndi yothokoza. **Tikupembedzani.**

Yesu mu Ukaristia, Nsembe yopepesa ndi yotinenera **Tikupembedzani.**

Yesu mu Ukaristia, Malo okhalira Mulungu pakati pathu **Tikupembedzani.**

Yesu mu Ukaristia, Buledi wamoyo wochokera kumwamba **Tikupembedzani.**

Yesu mu Ukaristia, Mana wobisika ndi wokoma **Tikupembedzani.**

Yesu mu Ukaristia, Mwanawankhosa weniweni wa Pasaka **Tikupembedzani.**

Yesu mu Ukaristia, Chuma cha Ansembe **Tikupembedzani.**

Yesu mu Ukaristia, Chuma cha akhristu **Tikupembedzani.**

Yesu mu Ukaristia, Kamba wa paulendo wa Mpingo **Tikupembedzani.**

Yesu mu Ukaristia, Mankhwala opatsa moyo wosatha **Tikupembedzani.**

Yesu mu Ukaristia, Chinsinsi cha chikhulupiriro **Tikupembedzani.**

Yesu mu Ukaristia, Mphamvu ya chiyembekezo **Tikupembedzani.**

Yesu mu Ukaristia, Chimangirizo cha chikondi **Tikupembedzani.**

Yesu mu Ukaristia, Gwelo la umodzi ndi mtendere **Tikupembedzani.**

Yesu mu Ukaristia, Kasupe wa chimwemwe choona **Tikupembedzani.**

Yesu mu Ukaristia, Sakramenti losungitsa uvirgo

**Tikupembedzani.**

Yesu mu Ukaristia, Sakramenti lotipatsira mphamvu

**Tikupembedzani.**

Yesu mu Ukaristia, Kulawa kwa phwando la kumwamba

**Tikupembedzani.**

Yesu mu Ukaristia, Chitsimikizo cha kuuka kwathu kwa akufa

**Tikupembedzani.**

Yesu mu Ukaristia, Chitsimikizo cha ulemerero wa mtsogolo

**Tikupembedzani.**

Kankhosa ka Mulungu amene mumachotsa machimo a dziko lapansi.

**Mufafanize machimo a anthu onse**

Kankhosa ka Mulungu amene mumachotsa machimo a dziko lapansi.

**Mutichitire chifundo Ambuye**

Kankhosa ka Mulungu amene mumachotsa machimo a dziko lapansi.

**Mutipatse mtendere.**

Tipemphere: Mulungu Atate athu, mogwirizana ndi akhristu onse a m'dziko la pansi pano, tikukuyamikani chifukwa, mwa Mwana wanu Yesu Khristu mu Ukaristia, simuleka kudyetsa mbumba yanu kuti ikhale yangwiro ndi yolumikizana m'chikondi chanu. Mutipatse mtima wolakalaka kukhala nawo Ukaristiawu, kuti tipezemo mphamvu. Mwa Yesu Khristu, Ambuye athu.

**Onse:** Amen.

## 17. Kupempherera mtendere

**Wansembe:** Mulungu Atate achisoni ndi achifundo, amene pa nyengo zonse ndi pa malo ponse mumatsogolera anthu anu. Tikukupemphani kuti m'dziko lathu lino ndi m'dziko lonse lapansi mukhale mtendere. Muthawitse m'dima wonse wa zoipa, chotsani mafunde onse obwera chifukwa cha kusiyana kwa maganizo, poletsani zilonda za udani ndi mantha, ndipo mutsogolerere atsogoleri athu kuti atsate njira ya chilungamo ndi umodzi. Chotsani khungu lonse m'maso mwathu kuti tizitha kuona anzathu ngati abale ndi alongo aulemerero wofanana. Lolani kuti chikondi chathu chikhale champhamvu kupambana zipolowe ndi kugawikana, ndipo chiyembekezo chidzaze mu mtima mwa munthu aliyense. Lolani kuti mtendere uyambike ndi ife kuti tikhale zida zodzetsa mtendere kwa ena. Mwa Yesu Khristu, Ambuye athu.

**Onse:** Amen.

### Pemphero la Fransisko wa ku Asisi

**Wansembe:** Ambuye,
**Onse:** ndikhale wodzetsa mtendere wanu.

**Wansembe:** Pamene pali chidani,
**Onse:** ndiikepo chikondi

**Wansembe:** Pamene pali kunyozana,
**Onse:** ndiikepo chikhulupiriro

**Wansembe:** Pamene pali kupeneka,

**Onse:** ndiikepo kumvera

**Wansembe:** Pamene pali kunyozana,
**Onse:** ndiikepo chikhulululukiro

**Wansembe:** Pamene pali mdima,
**Onse:** ndiikepo kuwala

**Wansembe:** Pamene pali chisoni,
**Onse:** ndiikepo chimwemwe

**Wansembe:** Ambuye Mulungu wanga,
**Onse:** mundipatse mtima wosakonda kungolandira chisangalatso koma makamaka woyesa kusangalatsa ena, wosafuna kuti ena azingotsata zanga zokha koma wotsata za ena, wosafuna kundikonda koma kukonda ena. Popeza kuti pakupatsa ndipo pamene timalandira, Pakukhululuka ndipo pamene timakhululukidwa, Pakufa ndipo pamene timabadwira ku moyo wosatha. **Amen.**

**Wansembe:** Mikaele Arkanjelo Woyera.
**Onse:** Mukhale mtetezi wathu!

**Wansembe:** Maria, Mfumukazi ya mtendere.
**Onse:** **M**utipempherere ife!

**18. Pemphero la Atate athu**

**19. Pemphero la Ulemu**

## 20. Mwambo wa Udalitso

*Onse agwada pamene wansembe ndi omuthandizira apita kukagwada pafupi ndi guwa la Ukaristia*

### i. Kupempherera Papa......:

***(Onani m'Buku la Nyimbo ndi Mapemphero kuchokera pa tsamba 275, No. 237).***

*Wansembe atsogolera pemphero lopempherera Papa motere:*

**Wansembe:** Tipempherere Papa wathu ........

**Onse:** Ambuye asunge iye, namkhalitsa ndi moyo, namdalitse m'dziko la pansi pano, ndi kumleretsa kwa zonyenga za adani ake.

**Wansembe:** Ndiwe thanthwe

**Onse:** Ndipo pa thanthwe ili, ndidzamanga Eklezia wanga.

**Wansembe: Tipemphere:**

Inu Mulungu, mbusa ndi muweruzi wa akhristu onse, muyang'ane ndi chifundo nduna yanu Papa .......... amene mwamsankhula kuti akhale wolamulira Eklezia wanu. Tikupemphani kuti, ndi maphunzitso ake ndi chitsanzo chake chokoma, mumthandize kuti athe kupulumutsa anthu ake onse, kuti pamodzi ndi msambi umene mwamsungitsa, alowe nawo ku moyo wosatha. Mwa Yesu Khristu Ambuye athu.

**Onse:** Amen.

**ii. Nyimbo ya Udalitso / yolemekeza Sakramenti:**

*Akhristu atsogolera nyimbo ya Udalitso kuchokera* ***m'Buku la Nyimbo ndi Mapemphero pa tsamba 276, No. 238, vesi 5 ndi 6****. Pa vesi 6 wansembe aima ndi kuika lubani m'chombo ndipo agwadanso ndi kufukiza.*

5. Sakramenti lopambana,
Tilipembedze tonse.
Pano pali mwambo wina,
Watha mwambo wakale.
Tivomere osakana,
Chimene sitiwona.

6. Kwa Atate ndi kwa Mwana,
Kukhale kwaulemu.
Tiwatame kopambana,
Tiwathokoze ndithu.
Tisaleke kutamanda,
Mlungu Mzimu Woyera. Amen.

*Atafukiza ndipo nyimba itatha, wansembe aimba mau motere:*

**Wansembe:** Mwawaninkha chakudya chakumwamba (Aleluya)

**Onse:** Chimene chili nazo zokondwetsa zonse. (Aleluya)

### iii. Pemphero

*Pambuyo pake wansembe aima ndi kunena pemphero lotsatirali. Pa nthawiyi, m'modzi mwa otumikira ku guwa apita kukatenga Humeral Veil pa Credence table.*

**Wansembe: Tipemphere:**

Inu Mulungu mudatisiira chikumbutso cha kufa kwanu, m'Sakramenti lanu lodabwitsa ndithu. Tikupemphani, mutiphunzitse ife kulemekeza Sakramenti la Thupi lanu ndi Magazi anu, kotero kuti, tilandire kosalekeza zabwino za chipulumutso chanu. M'dzina la Yesu Khristu Ambuye athu.

**Onse:** Amen

### iv. Kudalitsa anthu onse ndi Ambuye Yesu wokhala mu Ukaristia:

*Pambuyo pa pemphero, wansembe agwada ndipo otumikira ku guwa ampatsira '**Humeral Veil'** kuchokera kumbuyo kwake. Kenaka adzuka ndi kupita ku guwa ndipo atapereka ulemu anyamula **'Monstrance'** ndikudalitsa akhristu ndi Ukaristia. Pamene wansembe akudalitsa ndi Ukaristia, akhristu adzilemba chizindikiro cha mtanda.*

### v. Nyimbo ya matamando

*Pambuyo podalitsa akhristu ndi Ukaristia, wansembe abwerera pa chipata cholowera ku guwa, agwada ndipo otumikira ku guwa alandira **'Humeral Veil'** nkukaisiya pa **'Credence table'**. Kenaka, akhristu atsogolera nyimbo ya matamando kuchokera **m'Buku la Nyimbo ndi Mapemphero pa tsamba 278, No. 239 – 'Titamande Mulungu'.***

**TITAMANDE MULUNGU (No. 239)**

| | |
|---|---|
| Titamande | Mulungu. |
| Titamande | Dzina lao Loyerayera. |
| Titamande | Yesu Khristu Mulungu ndi munthu pamodzi. |
| Titamande | Dzina la Yesu. |
| Titamande | Mtima wake Woyerayera. |
| Titamande | Magazi ake Oyerayera. |
| Titamande | Yesu M'Sakramenti Loyera la Ukaristia. |
| Titamande | Mzimu Woyera Msangalatsi. |
| Titamande | Amai a Mulungu, Maria Woyerayera. |
| Titamande | Maria Woyera, Wopanda tchimo lobadwa nalo. |
| Titamande | Maria, Womkweza mwaulemu kumwamba. |
| Titamande | Dzina la Maria, Amai ndi Virgo. |
| Titamande | Yosefe Woyera, Mwamuna wao Woyerayera. |
| Titamande | Mulungu chifukwa cha Angelo ndi Oyera ake. |

**Kapena**

**TAMANDANI AMBUYE (240)**
Tamandani Ambuye mafuko onse
Tamandani Iye makamu onse.
Chifukwa chifundo chao chalimbitsira ife,
Ndi mau Ambuye ngoona nthawi zonse.

Ulemu ukhale kwa Atate ndi kwa Mwana,
Ndi kwa Mzimu Woyera,
Monga panali poyamba ndi tsopano ndi masiku onse
Ndi pa nthawi zosatha. Amen.

**vi. Kuchotsa pa guwa Ambuye Yesu wokhala mu Ukaristia**

*Pambuyo pa nyimbo ya 'Titamande Mulungu', onse ali chigwadire, wansembe apita ku guwa ndipo atapereka ulemu, achotsa Ukaristia mu **'Monstrance'** ndikukabwezeretsa m'tebenakulo.*

**21. Nyimbo yotulukira ya Amai Maria**

*Atabwezeretsa Ukaristia m'tebenakulo, wansembe aika **'Monstrance'** pa malo ake ndi kupinda **'Corporal'** ndipo apsopsona guwa ndi kupita pa chipata cholowera ku guwa, apereka ulemu pamodzi ndi otumikira ku guwa ndipo akhristu aima ndi kutsogolera nyimbo yotulukira.*

**18:45 - 19:45 hrs.:** **Chakudya cha madzulo**

**19:45 hrs.:** **Kupembedza motsogoleredwa ndi Catholic Charismatic Renewal**

*Gulu la Catholic Charismatic Renewal liyendetsa mwambo wopembeda wa usiku motsogoleredwa ndi Bambo Mlangizi wao. Ansembe, asisitere, a brother, a catechist ndi akhristu onse akulimbikitsidwa kukhala nao pa mwambowu kufikira pamene iwo afuna kupita kukagona kuti akapumulire.*

**DAY TWO: Friday, 4th September, 2026:** **Zokambirana, Nsembe ya Ukaristia ndi Mdipiti woyenda ndi Sakramenti Loyerayera la Ukaristia**

**8:00 – 9:00 hrs.:** **Mutu wachitatu –** Sr. Elizabeth Namuthuwa, SDP

"Eucharist at the centre of consecrated life and our devotion to the Blessed Sacrament." / "Ukaristia ngati gwero la moyo wathu wauzimu komanso kupembedza Ambuye Yesu okhalamo."

**9:00 – 9:30 hrs.:** **Kukambirana za mutu wachitatu**

**9:30 – 10:30 hrs.:** **Mutu wachinai –** Rev. Fr. Stanford Sungani, DP

"Sacrament of Penance and Reconciliation as preparation for the Eucharist." / "Kulapa ndi Kuyanjana ngati njira yokonzekera bwino pokalandira Ukaristia."

**10:30 – 11:00 hrs.:** **Kukambirana za mutu wachitatu**

**11:00 – 11:15 hrs.:** **Sakramenti la kulapa ndi kukonzekera Nsembe ya Ukaristia.**

*Onani Mapemphero okonzekera Nsembe ya Ukaristia pa tsamba 29.*

**11:15 – 12:00 hrs.** **Nsembe ya Ukaristia**

*Mau a Mulungu akuchokera pa Lachisanu, Mulungu wa 22 pa chaka*

**Mau oyamba:** 1 Akorinto 4:1-5

**Nyimbo ya Salimo:** Salimo 37:3-6. 27-28. 39-40

**Mthenga Wabwino:** Luka 5:33-39

**12:00 – 13:00 hrs.:** **Lunch Break**

**13:00 – 14:00 hrs.:** **Mutu wachisanu:** Rev. Fr. Cosmas Kinly, DP

*"The Holy Eucharist with Family Life."*

**14:00 – 14:30 hrs.:** **Kukambirana za mutu wachisanu**

**14:30 hrs.:** **Kukonzekera mdipiti wa Ukaristia**

**15:00 hrs.:** **Mdipiti wa Ukaristia kuchokera pa Jubilee Square, Chikwawa Cathedral kupita ku St. Lawrence Girls Catholic Secondary School.**

**Dongosolo lotsekulira ndi kuyenda ndi Sakramenti Loyerayera la Ukaristia**

i. Akwaya atsogolera nyimbo ya Ukaristia pamene wansembe afika ku guwa pamodzi ndi omuthandizira. Kenaka, onse agwada pamene wansembe aika Ukaristia pa guwa.
ii. Onse ali chigwadire, wansembe afukiza
iii. Onse asinkhasinkha pang'ono
iv. Mdipiti uyamba potsata dongosolo motere:

(Achipembedzo awiri olondolera othandizira Misa ndi ansembe.)

1. Wonyamula mtanda ndi amakendulo.
2. Othandizira Misa ena

3. Ansembe onse
4. Wonyamula chombo ndi lubani
5. Wansembe atanyamula Ukaristia

(Achipembedzo awiri olondolera ana a maluwa)

6. Ana a maluwa

(Achipembedzo awiri olondolera asisitere)

7. Asisitere

(Achipembedzo awiri olondolera kwaya yotsogolera.)

8. Kwaya imene ikutsogolera pa m'dipiti woyenda ndi Ukaristia

(Achipembedzo awiri olondolera akhristu onse.)

9. Akhristu ena onse m'magulu osiyanasiyana akuimba nyimbo za Ukaristia mosangalala ndi mwaulemu. Angathenso kumachita mapemphero osiyanasiyana malinga ndi magulu awo achikhristu.

**Zochitika pa mdipiti woyenda ndi Sakramenti Loyerayera la Ukaristia.**

i. Kukwera galimoto:

*Wansembe atatuluka pa chipata cha Jubilee Square, akwera galimoto limene lakonzedwa. Patsogolo pa galimoto yonyamula Ukaristia pakhalanso galimoto zina. Ndondomeko ya galimoto ili motere:*

1. Galimoto yonyamula chimkuza mau
2. Galimoto yonyamula wojambula mwambo

3. Galimoto yonyamula wa mtanda
4. Otumikira ku guwa oyenda pansi
5. Ansembe onse oyenda pansi
6. Galimoto yonyamula ansembe ena
7. Galimoto ya Episikopi
8. Anyamata anai onyamula makandulo oyaka
9. Wa chombo ndi lubani / belu oyenda pansi
10. Galimoto yonyamula Ukaristia
11. Galimoto yonyamula ana a maluwa
12. Galimoto yonyamula asisitere ena
13. Asisitere onse oyenda pansi
14. Catholic Charismatic Renewal ovala makaka ao
15. CFM ovala makaka ao
16. CWA ovala makaka osiyanasiyana m'magulu m'magulu
17. Legion of Mary ovala makaka ao
18. A Franciscan ovala makaka ao
19. A St. Vincent de Paul ovala makaka ao
20. Makwaya osiyanasiyana ovala makaka ao
21. YCW ovala makaka ao
22. CMA ovala makaka ao
23. Makwaya osiyanasiyana ovala makaka ao
24. YCS ovala makaka ao
25. Akhristu ena onse
26. Galimoto yonyamula akhristu omwe sangathe kuyenda pansi

ii. Mwambo wa Udalitso woyamba pa CADECOM:

*M'dipiti uyenda ndipo wansembe wonyamula Ukaristia atafika pa Ofesi ya Directorate of Social Services / CADECOM aima pa malo pamene pakonzedwa bwino ndipo*

*adikira anthu onse kuti afike. Onse atafika, mwambo wa Udalitso woyamba uyambika motere:*

- Akwaya atsogolera nyimbo ya Ukaristia mavesi awiri
- Wansembe atsogolera kunena kapena kuimba pemphero lopempherera a Papa. (*Onani m'bukuli pa tsamba 17 kapena m'Buku la Nyimbo ndi Mapemphero pa tsamba 275, No. 237)*

*Mwambo wa Udalitso upitirira monga nthawi zonse. Pambuyo pa Udalitso,* ana a maluwa agwada ndi kupembedza powaza maluwa mwaulemu akuimba nyimbo, **'Ambuye anga ndi Mulungu wanga, ndikupembedzani'**. Pambuyo pake mdipiti upitirira.

iii. Mwambo wa Udalitso wachiwiri pa GROUND YA CHIKWAWA SECONDARY SCHOOL:

*M'dipiti uyenda ndipo wansembe wonyamula Ukaristia atafika pa* ground ya Chikwawa Secondary School, *aima pa malo pamene pakonzedwa bwino ndipo adikira anthu onse kuti afike. Onse atafika, mwambo wa Udalitso wachiwiri uyambika motere:*

- Akwaya atsogolera nyimbo ya Ukaristia mavesi awiri
- Wansembe atsogolera kunena kapena kuimba pemphero lopempherera a Papa. *(Onani m'bukuli pa tsamba 17 kapena m'Buku la Nyimbo ndi Mapemphero pa tsamba 275, No. 237)*

*Mwambo wa Udalitso upitirira monga nthawi zonse. Pambuyo pa Udalitso,* ana a maluwa agwada ndi kupembedza powaza maluwa mwaulemu akuimba nyimbo, **'Ambuye anga ndi Mulungu wanga, ndikupembedzani'**. Pambuyo pake mdipiti upitirira.

iv. Mwambo wa Udalitso wachitatu pa ST. LAWRENCE GIRLS CATHOLIC SECONDARY SCHOOL:

*M'dipiti uyenda ndipo wansembe wonyamula Ukaristia atafika pa* St. Lawrence Girls Catholic Secondary School, *asiya Ukaristia pa guwa limene lakonzedwa bwino ndipo adikira anthu onse kuti afike. Onse atafika, mwambo wa Udalitso wachitatu uyambika motere:*

- Akwaya atsogolera nyimbo ya Ukaristia mavesi awiri
- Wansembe atsogolera kunena kapena kuimba pemphero lopempherera a Papa. *(Onani m'bukuli pa tsamba 17 kapena m'Buku la Nyimbo ndi Mapemphero pa tsamba 275, No. 237)*

*Mwambo wa Udalitso upitirira monga nthawi zonse. Pambuyo pa Udalitso,* ana a maluwa agwada ndi kupembedza powaza maluwa mwaulemu akuimba nyimbo, **'Ambuye anga ndi Mulungu wanga, ndikupembedzani'**.

v. Kubwezeretsa Sakramenti Loyerayera la Ukaristia

*Ana a maluwa atapembedza, Wansembe abwezeretsa Ukaristia m'galimoto ndipo pakhala kutsazikana.*

vi. Kutsazikana

*A Pastoral Secretary athokoza anthu onse ndi kuwafunira madzulo abwino. Anthu onse achoka pa St. Lawrence Girls Catholic Secondary School kupita ku nyumba kwao kapena ku malo kumene akugona motere:*

- Galimoto yonyamula Ukaristia
- Galimoto ya Episikopi.
- Galimoto ya ansembe
- Galimoto ya asisitere
- Ena onse.

**DAY THREE: Saturday, 5th September, 2026: Mwambo wotsekera Msonkhano Waukulu wa Ukaristia**

**8:00 – 8:45 hrs.:** **Kupemphera kolona ya Amai Maria – wotsogolera a Legio ya Amai Maria**

**8:45 – 9:15 hrs.:** **Kulengeza mfundo zikuluzikulu zomangidwa pa msonkhano waukulu wa Ukaristia**

**9:15 – 9:30 hrs.:** **Sakramenti la kulapa ndi kukonzekera Nsembe ya Ukaristia –**

*Onani Mapemphero okonzekera Nsembe ya Ukaristia pa tsamba 29.*

**9:30 – 11:00 hrs.:** **Nsembe ya Ukaristia yotsekera msonkhano waukulu wa Ukaristia**

*Mau a Mulungu akuchokera pa Loweruka, Mulungu wa 22 pa chaka*

**Mau oyamba:** 1 Akorinto 4:6-15

**Nyimbo ya Salimo:** Salimo 145:17-21

**Mthenga Wabwino:** Luka 6:1-5

**11:00 – 11:30 hrs.:** **Nthumwi za ku msonkhano zipatsidwa ntchito ndi kutumidwa.**

**11:30 – 12:00 hrs** **Kutola zithunzi**

**12:00 – 13:00 hrs** **Chakudya chamasana ndi kutsazikana**

**Mapemphero okonzekera Nsembe ya Ukaristia**

1. Chizindikiro cha mtanda
2. Atate athu
3. Tikuoneni Maria
4. Kulapa
5. Kukonda
6. Kupempherera anthu onse
7. Kukhulupirira
8. Ulemu

9. Pemphero la Yohane Chrysostom Woyera (Musanayambe Misa)

Ndikukhulupirira, Ambuye, ndipo ndikuvomereza kuti Inu ndinu Khristu weniweni, Mwana wa Mulungu Wamoyo, amene munabwera padziko lapansi kudzapulumutsa ochimwa, ndipo ine ndine m'modzi wa iwo.

Ndipo ndikukhulupirira kuti Ukaristia ndi Thupi Lanu loyera ndi Magazi Anu amtengo wapatali. Choncho, ndikupemphani, ndichitireni chifundo ndipo mundikhululukire machimo anga—kaya ndinawachita mwadala kapena mosadziwa, m'mawu kapena m'zochita, kaya ndikuwadziwa kapena sindikuwadziwa. Ndipo mundipatse mwayi wolandira Chakudya choyerachi popanda kundiweruza, kuti ndiyeretsedwe ndipo ndikhale ndi moyo wosatha. Amen.

10. Chizindikiro cha mtanda.